

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

“CHOYAMBIRIRA YERETSANI”

Yesu anawayang'ana alembi ndi afarisi nawadzudzula kuti: “Mutsuka kunjwa kwake kwa chikho ndi mbale, koma m'katimo mwadzala ndi kulanda ndi kusadziletsa... yambotsuka m'kati mwa chikho ndi mbale, kuti kunjwa kwake kukhalenso koyera. Chomwecho inunso muonekera olungama pamaso pa anthu, koma m'kati muli odzala ndi chinyengo ndi kusaweruzika” (Mateyu 23:25-28).

Afarisi amavala mwakuti awonekere pamaso pa anthu ngati olungama ndi achiyero. Yesu anadziwa mitima yawo ndipo anawalamula kuti “ayeretse kaye” munthu wamkatiyo. Chofunikira koposa mtundu wa chovala ndi mmene ulili mtima wathu pamaso pa Mulungu. Anthu ena masiku ano akuchita monga momwe amachitira Afarisi akalewo amene amadziyesa okha olungama. Chifukwa cha ichi, iwo amafuna kulungamitsidwa kuchokera ku mavalidwe awo abwino ndi aulemu komanso kulemekezidwa. Yesu analamula kuti si zinthu zakunja zimene zimayipitsa munthu koma ndi izo zimene: “zichokera mumtima” (Mateyu 15:17-20). Ngati mtima si wolungama pamaso pa Mulungu, zonse zochitika kunjwa zikhala zopanda pake.

Chochitika kunjwa pofuna kubisa kusalungama kwa mkati chimatchedwa kuti chiphamaso.

Khristu sanatsutse kufunikira kwa kuvala modzilemekeza. Koma mmalo mwake anatsindika mfundo yakuti choyambirira



mtima ndi umene uyenera kutsukidwa, kenaka zakunja nazonso zitsukidwe. Kudzilemekeza ndi kuvala mwa umulungu zimaperkedwa kwa munthu ngati chilungamo pokhapo pamene chile chipatso cha mtima woyera. Anthu sapulumutsidwa kapena kulungamitsidwa chifukwa cha ntchito zawo koma chifukwa cha chisomo chochita mwa chikhulupiriro (Aefeso 2:8-9). Munthu amene mtima

wasinthika kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu, mwana wa Mulungu ayenera kutsata chiyero mu gawo lililonse la moyo wake, apo bii sadzaona Ambuye (Ahebri 12:14).

Kupulumutsidwa kwa mzimu kumabweretsa kusintha kwakukulu. “Koma tsopano, pamene munamasulidwa kuuchimo, ndi kukhala akapolo a Mulungu, muli nacho chobala chanu chakufikira chiyeretso, ndi chimariziro chache moyo wosatha” (Aroma 6:22). Uchimo, kudzikuzi, kusisira koipa, ndi chidetsa ziyeretsedwe ndi kuchotsedwa. “Mukonzeke, mukhale atsopano mu mzimu wa mtima wanu, nimuvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m'chilungamo, ndi m'chiyero cha choonadi” (Aefeso 4:21-24).

Ukulu wa malemba umatsindika pa kufunikira kwa munthu wamkati, popeza pamene munthu wamkati akhala mofanizidwa ndi Mzimu wa Khristu, chipatso chotsatira choonekera kunjwa chimakhala choyera. Baibulo silinena gawo lililonse la moyo, komabe limanena mfundo zoyenera kuti tilemekeze Mulungu. Maziko

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mawu a Mkonzi

Maonekedwe Akunja

Mavalidwe a Chikhristu

Chikhalidwe

Kodi Mukudziwa?

Utsogoleri

9

Mau a pa Nyengo yake

3

4

5-9

Mafunso ndi Mayankho
10-11

12

ZIMENE BAIBULO Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

amene timapanga ziganizo za mavalidwe ndi chikhalidwe akuyenera kukhazikika pa mfundo zoyera za Mau. Pamene anthu adziko amangodalira zimene amaganiza naysa kudzilungamitsa okha, Mzimu adzatsogolera mosamulakwitsa munthu aliyense woona mtima amene akufuna chitsogozo chenicheni.

Mulungu wa Kumwamba amakhala mwa iwo amene ali ake “Pakuti atero Iye amene ali wamtali wotukulidwa, amene akhala mwachikhalire, amene dzina lake ndiye Woyera, Ndikhala m’ malo atali ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali wa mzimu wosweka ndi wodzichepetsa, kutsitsimutsa mzimu wa odzichepetsa, ndi kutsitsimutsa mtima wa osweka” (Yesaya 57:15). Mtumwi Petro analangiza mwana wa Mulungu kuti “muvale kudzichepetsa kuti mutumikirane; pakuti Mulungu akaniza odzikuza, koma apatsa chisomo kwa odzichepetsa” (1 Petro 5:5). Monga mtima umakhala wodzichepetsa pamaso pa Mulungu, chomwechonso munthu wamkati ayenera kuwonetsera kudzichepetsa kwa mkati. “Koma kukhale munthu wobisika wamtima, m’chovala chosaola cha mzimu wofatsa ndi wachete, ndiwo wa mtengo wake wapatali pamaso pa Mulungu” (1 Petro 3:4).

Chiyero ndi chokongola pamaso pa Ambuye. Iye ayenera kulambiridwa ndi kulemekezedwa mu kachisi wa mtima wathu amene ali woyera ndi wodzikhuthula. “Kapena simudziwa kuti thupi lanu lili kachisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m’thupi lanu” (1 Akorinto 6:19-20).

—mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m’ dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata yu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawa amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & René Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m’maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Okonedwa, pakuchita changu chonse chakukulemberani za chipulumutso cha ife tonse, ndafulumidwa mtima ine kukulemberani ndi kudandaulira kuti mulimbanetu chifukwa cha chikhulupiriro chapatsidwa kamodzi kwa oyera mtima. —Yuda 1:3

Mtolo wa katundu mu kalata ya ulendo uno uli pa mutu wa: “Maonekedwe akunja kapena Mavalidwe a Chikristu.” Mulungu akadali ndi muyeso wa kavalidwe, ndipo izi sizitengera kuti ambiri akutsata mavalidwe a dziko lapansi. Kusiyana kwake kwa anthu a Mulungu ndi anthu achikunja kupitirira pamene uchimo udzakhala ukuchuluka mmasiku ano omaliza. Ambuye atithandize kuti tigwiritsitse chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kudzera mu Mau a Mulungu. Ndikufuna kulimbikitsa owerenga aliyense kuti agwiritsitse chiphunzitso ichi choona. Ngati pali zinthu zimene simumvetsetsa, musamale kuti musachotse ziphunzitso zakalekale zimene zakhazikika kwa nthawi yonse.

Zisomo za munthu wamkatiyo ndi zofunikira kuposa zooneka kunja. Chimakhala chinthu chamanyazi kuona anthu akudzitamandira kuti ndi aulemu koma moyo wao ndi wachikunja, wodzitukumula ndi wosowa chikondi. Komabe moyo woonekera kunja ndi gawo limodzi la moyo ndipo malemba amanenapo za moyo umenewu. Chilichonse chimene timachita chidzikhala chokhudzana ndi ubale wathu ndi Ambuye.

Nthawi zambiri anthu amakhumudwa pamene akulalikira za maonekedwe akunja, makamaka akamatchula tchutchutchu wake. Zimakhala zomvetsa chisoni pamene anthu amene amakhulupirira mu kukhala moyo wachiyero asakufuna kukamba nkhani za mavalidwe. Inde pamafunikira nzeru, komabe sikuti pamachita kukhala nthawi yake yoyenera. Kodi anthu angadziwe bwanji za dongosolo la Mulungu pa moyo wao ngati sanaphunzitsidwe? Pamene anthu ambiri akhala m’ moyo wachikunja, ndikovuta kwambiri kuti abusa aphunzitse za nkhanayi. Zinthu zina zimaoneka ngati zosafunikira, ndipo ambiri amanena kuti zilibe ntchito, koma pamene anthu ayamba kulolera kuti tinthu ting’ onoting’ono tiyambe kuwasokoneza, mapeto ake limakhala vuto lalikulu ku uzimu.

Ndimakumbukira za nkhani ya taye mu mpingo wa Church of God. Panali kugawanikana mzaka za 1910-1913 pamene imodzi mwa nkhani zake inali ya taye. Ena samafuna kuvomereza zakuti taye idzivalidwa mkhosi imene cholinga chake sichimadziwika bwino. Ena anafuna kuti idzivalidwa kuti afanane ndi ena onse. Ngakhale chinali chinthu chaching’ono mwa icho chokha, anthu amene ankambikira zakuti taye idzivalidwa posakhalitsa anayamba kutayilira pa zinthu zina zokhudzana ndi choonadi. Ndipo lero pakati pawo palibe muyeso weniweni wokhazikika kuchokera mu Baibulo wokhudzana ndi kuvala moyenera. Pamene tikunena za taye kapena mkanda wa mkhosi, cholinga chake ndi chiyani? Mfundo yeniyeni, chimene chikupangitsa komanso cholinga cha chinthu chimakhala chofunikira kwambiri kuposa chinthucho kapena chovalacho.

Sitikufuna kuti tikodwe mu msampha wa chilamulo kapena kutengeka koma tikufuna kuti tikhale m’ moyo wauzimu wosatekeseka. Pakati pa oyera mtima, pakhoza kukhala kusiyana pa zinthu zina ndi zina zazing’ono zoonekera kunja, komabe sindikhulupirira kuti tidzatalikana kwambiri ngati tonsefe tidzatsatira mfundo zoonza za Mau a Mulungu. Chidzakhala chinthu chodala pamene tikhala mmoyo wodzichepetsa ndi waulemu mwa Yesu Khristu. Ambuye atipatse tonsefe mtendere ndiponso kulimbika mtima kuti tiyime chilili mu dziko lino la mdima ndi kukhala moyo wokondweretsa Mpulumutsiyo.

Michael W. Smith

April 2016

Zambiri Zili pa

INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone. makalata akale.



TAKULANDIRANI

Anthu oyera mtima a Mulungu amalandira ku zipembedzo zawo anthu amene sakufikapo pa muyeso wa Baibulo wa kuvala moyenera.

UTSOGOLERI

Molingana ndi Malemba ndi koyenera kuti iwo amene ali utsogoleri akhale mmoyo wopanda banga ndikuti akhale chitsanzo kwa gulu la nkhosa limene akuliyang'anira mu gawo lililonse la moyo wawo. Abusa, aphunzitsi a Sande Sukulu, utsogolera nyimbo, ndi atumiki akuyenera kuvala, osati pa chipembedzo pokha koma kwina kulikonse, mu njira imene imakhala ya chiyero. Kulephera kukhala mu ziphunzitsi izi za Malemba kumapangitsa kuti munthu asakwanire pa udindo wa utsogoleri.

KUSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: MAONEKEDWE AKUNJA

Kuwerenga Malemba: Kapena simudziwa kuti thupi lanu lili Kachisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu. —I Akorinto 6:19-20

Chidule: Anthu oyera mtima a Mulungu akuyenera kuvala moyenera, mwaulemu ndi modzile-mekeza ndipo asavale ndolo ndi zibangili zokometsera komanso zodzoladzola. Maonekedwe akunja akhale choonetsera cha kudzichepetsa ndi chiyero chamkati.

I. Kufunikira kwa Munthu Wakunja

- A. 1 Samuele 16:7 Munthu amayang'ana maonekedwe akunja.
- B. Mateyu 5:14-16 Inu ndinu kuunika kwa dziko.

II. Munthu Wamkati

- A. Mateyu 15:17-20 Zinthu zimene zimayipitsa.
- B. Yesaya 57:15 Mtima wosweka ndi wodzichepetsa.
- C. 1 Petro 5:5 Muvale kudzichepetsa.
- D. 1 Petro 3:4-5 Munthu wobisika wa mumtima.

III. Zinthu zoyamba Zikhalebe Zoyamba

- A. Aefeso 2:8-10 Kupulumutsidwa mwa chisomo kuti muchite ntchito zabwino.
- B. Mateyu 23:25-28 Yeretsani kaye *chimene* chili mkati.

IV. Kuyitanidwa ku Chiyero

- A. Ahebrei 12:14 Tsatani chiyero.
- B. Eksodo 6:22 Chipatso cha ku chiyero.
- C. Aefeso 4:21-24 Valani munthu watsopano.
- D. 1 Petro 2:9 Fuko losankhika, anthu akeake.

V. Muyeso wa Baibulo wa Kavalidwe

- A. Genesis 3:7-10, 21 Mulungu anaveka Adamu ndi Hava.
- B. Yesaya 47:2-3 Chipangano Chakale – chionetsero cha kusavala.
- C. Yohane 21:7 Kusavala kwa Petro.

- D. Duteronomo 22:5 Amuna komanso akazi ali ndi chovala chawochawo.
- E. 1 Timoteo 2:9 Chovala chakunja chaulemu ndi chosachititsa manyazi. (1 Petro 3:3).
- F. 1 Timoteo 4:12 Chitsanzo cha chiyero.

VI. Zinthu za Dziko lino

- A. Aroma 12:2 Musafanizidwe ndi dziko lapansi.
- B. 1 Yohane 2:15-17 Musakonde dziko lapansi.

VII. Zodzoladzola ndi Zokometsera ngati zibangili, ndolo

- A. 1 Timoteo 2:9-10 Zokometsera zikuletsedwa. (1 Petro 3:3).
- B. Yesaya 3:16-24 Maweruzo a Mulungu. (Yeremiya 4:30).

VIII. Tsitsi

- A. 1 Akorinto 11:14-15 Kutalika.
- B. 1 Timoteo 2:9, 1 Petro 3:3 Likonzedwe mosadzikometsera kwambiri.

IX. Muyeso wa Kuweruza

- A. 2 Akorinto 10:12, 18 Iye amene Ambuyey amuvomereza.
- B. Yohane 12:48 Kuweruzidwa ndi Mau.
- C. Yesaya 62:10 Muyike muyeso pakati pa anthu.
- D. 1 Yohane 5:3 Chikondi cha Mulungu.

Kumaliza:

Popeza Yehova akondwera nao anthu ake; adzakometsa ofatsa ndi chipulumutso.

—Salmo 149:4

Maonekedwe Akunja

Mavalidwe a Chikristu

Aulemu: Kudziletsa podziwa chimene iweyo uli, osati chothina kwambiri, osatinso chotaya kwambiri, Cholemekezeka, cha dongosolo, chabwino, osati chochita kunkitsa makongoledwe ake, chosaonetsera kulemera kwanu.

Abwino: Oonetsa kuti ndinu ofatsa ndi amakholidwe; oonetsa kuli ndi a siliasi, oonetsa kuti mutu wanu umaganiza bwino komanso mwanzeru.

Obisa manyazi: Odzilemekeza, odzipatsa ulemu kapena odzigwira.



Kuitanidwa kuchokera ku Mdimba

Mpingo wa Mulungu mu mbadwo uno ukadali mtundu wopatulika. Anthu a Mulungu ndi opatulika kuchoka ku dziko lapansi monga mmene aliri Khristu mwini wake koma si a dzikoli. Mwana aliyense wa Mulungu waitanidwa “Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za Iye amene anakuitanani mutuluke mumdimba, mulowe kuunika kwake kodabwitsa” (1 Petro 2:9). Umenewu si udindo chabe ayi, koma ndi mwayi kwa anthu a Mulungu kuti alole kuunika kwao kuwale kuti potero ena awone chiyero cha Mulungu (Mateyu 5:14-16). Ngakhale mipingo yambiri lero yazilala pa chiphunzitsa chopezeka m’Malemba cha kudzilemekeza ndi mavalidwe, Mau a Mulungu sanasinthe. Dziko limayika mtima kwambiri pa kufunikira kwa kavalidwe ndi kaonekedwe. Masiku ano, anthu ambiri akukakamidwa kuti avale potsatira fashoni kapena zovala zimene zimadinda thupi lawo lonse. Mau a Mulungu amapereka malangizo ndi chitsogozo pa nkhani zokhudza maonekedwe akunja.

Nchifukwa chiyani Mavalidwe ali ofunikira?

Chovala komanso maonekedwe akunja ndi ofunikira kwa anthu a Mulungu chifukwa Mulungu anati “Lemekezani Mulungu m’thupi lanu” (1 Akorinto 6:20). 1 Samuele 16:7 ndi vesi imene imatchulidwa kawirikawiri pofuna kutsimikiza kuti maonekedwe akunja alibe kanthu ngati mtima suli okonzeka: “pakuti munthu ayang’ana chooneka ndi maso, koma Yehova ayang’ana mumtima.” Pamene Mulungu ayang’anadi za mumtima, Akhristu akuitanidwa kuti akhale mboni kwa anthu amene sangaone za mumtima. Nthawi zambiri anthu amaweruzidwa molingana ndi zoonekera kunjira zimene nthawi

zambiri zimaonetsera zimene zili mumtima, zimene munthu amakhulupirira, zimene amaziyika pamwamba pa china chilichonse komanso mmene amadzionera. Zovala ndiponso maonekedwe a mwana wa Mulungu zionetsere ndi kupereka uthenga wa kudzichepetsa, chilungamo, ndi chiyero chimene Mulungu amafuna. Pamene oyera mtima sakuyenera kupembedza moyo wovala modzilemekeza, kuvala modzilemekeza kuchokere mu chiphunzitsa cha Mau a Mulungu, ndipo anthu ayenera kuchigwiritsa chimenechi.

Kodi Maliseche mu Baibulo ndi chiyani?

Pachiyambi penipeni, Adamu ndi Hava atachimwa, iwo anazindikira kuti anali amaliseche. Nthawi yomweyo iwo anafuna kuti adziphimbe ndi masamba a mkuyu ndipo anakabisala popeza amachita manyazi. Chimodzi chimene Mulungu anachita ndicho kuwasokera chovala cha chikopa kuti awaveke mokwanira (Genesis 3:7-10, 21). Mu Malemba maliseche sayimira kukhala osavala kokha. Yesaya 47:2-3 imalongosola kuti mzimayi amayesedwa wa maliseche ngati mwendo wake unali pamtunda ndipo ntchafu yake (kunena kuti kudutsa mawondo) zinali powonekera. Taganizirani za ophunzira uja Petro, amene amawedza. Pamene anamva kuti Ambuye ali pamene “anadziveka malaya a pathupi, pakuti anali wamaliseche, nadziponya yekha m’nyanja” (Yohane 21:7). Malingana ndi *Smith’s Bible Dictionary*, abambo ndi amayi a panthawi imeneyo onse ankavala chovala chamkati chogwira thupi chofanana ndi siketi yayitali. Mtundu wina wa chovala unali wodula manja ndipo chimaika m’mapondo, pamene mtundu wina wa chovala chamkati umafika mpaka m’mapondo ndi m’mapazi. Panali chovala chachiwiri

(Yapitirira pa tsamba 6)

Zovala komanso maonekedwe a mwana wa Mulungu aonetsere ndi kupereka uthenga wa kudzichepetsa, ungwiro ndi chiyero chimene Mulungu amachifuna.



(Kuchokera pa tsamba 5)

Muyeso wa
chovala kwa
mwana wa
Mulungu ndiwo
wa kudzilemekeza
ndi
kusadzikundikira.

chimene chimavaliwa kunja ndipo chinali chachitali kuposa chamkati chija. Anthu amatengedwa ngati ali maliseche akakhala kuti sanavale chovala chakunjacho. Nchifukwa chake, Petro, ngakhale anali ndi zovala zamkati zija, anachita changu kuvala chakunja chija kuti potero zioneke kuti wavala mokwanira (Onaninso 1 Samuele 19:24). Malemba awa amayamba powulula mmene Mulungu amaonera zokhudza umaliseche. Dzikoli ladzaza ndi anthu amene amavala makabudula aafupi, ma mini siketi kapenanso zina zazifupi. Izi ndi zosutsana kwambiri ndi Mau a Mulungu ndipo zimasutsana ngakhale ndi mu Chipangano Chakale mmene muyeso wa mavalidwe sunali waukulu monga mmene unaliri mu Chipangano Chatsopano.

Kusiyana pakati pa Amuna ndi Akazi

“Mkazi asavale chovala cha mwamuna, kapena mwamuna asavale chovala cha mkazi; pakuti aliyense wakuchita izi Yehova Mulungu wanu anyansidwa naye” (Duteronomo 22:5). Ngakhale malemba ali pamwambapa akunena makamaka za kuletsa akazi kutenga zida za ku nkondo, ndi chinthu chodziwika ndithu kuti Mulungu amadana ndi kusasiyanitsa pakati pa amuna ndi akazi. Chifukwa chakuti chikhalidwe cha makono chimavomereza mchitidwe wina wake, sizitanthauza kuti madalitso a Mulungu ali pa machitidwe amenewo. Mtundu wa mavalidwe uliwonse umene susiyanitsa pakati pa amuna ndi akazi ndi chinthu chonyansa pamaso pa Mulungu. Chikhalidwe chathu chikuyesetsa kufufuta maudindo amene Mulungu anakhazikitsa pakati pa amuna ndi akazi komanso ngakhale maonekedwe. Kuvala makabudula aafupi ndi ma thalauza kwa azimayi ndi zotsatira za akazi kusiya maudindo awo amene

Mulungu anawapatsa. Mchitidwe uwu sikuti umangotsutsana ndi dongosolo la Mulungu lokha, komanso umatsutsana ndi dongosolo lalikulu limene Mulungu anaika lokhudza maudindo a abambo ndi amayi kunyumba ndiponso m’dziko. Chimodzimidzi, masiku ano, pali mchitidwe komanso fashoni ya azibambo kuvala za chizimayi. Izinsu ndi zolakwika.

Tikulangizidwa kuti tivale modzilemekeza

Paulo anamupatsa Timoteo malangizo omveka bwino pa 1 Timoteo 2:9 za mmene mkazi wa umulungu ayenera kuvalira. “Momwemonso, akazi adziveke okha ndi chovala choyenera, ndi manyazi, ndi chidziletso; osati ndi tsitsi lake loluka, ndi golide kapena ngale, kapena malaya a mtengo wake wapatali.” Malemba akunena mwachimvekere ndipo akutanthauza zimene akunena kuti muyeso wa mavalidwe kwa mwana wa Mulungu ndiwo wovala modzilemekeza ndi mosadzikometsera kowirikiza. Pakati pa azimayi amene ndi a chikhristu kuvala kodzilemekeza ndi kosachititsa manyazi kulipo kochepe zedi. Abambo ndi amayi asamangothamangira kuti bolani abisa matupi awo, koma chovala chawo chidzikhala chaulemu ndi chokwanira bwino. Anthu akumavala zovala zimene zili zothina komanso zogwira thupi ndi kuonetsa zovala zamkati. Izi zisamachitike pakati pa anthu a Mulungu. Mkazi adzivala chovala chakunja chaulemu ndipo chimene chili chosachititsa manyazi. Masiketi kapena ma mini amene sapitirira m’kawondo amakhala osapatsa ulemu. Masiketi okhala ndi siliti yaitali kwambiri, ngakhale atakhala kuti ndi aatali ndithu, cholinga chake ndi kuti anthu aone mwendowo. Izinsu sizoyenera malingana ndi Mau a Mulungu.

Malemba amaletsa kuvala zovala zodula mtengo kwambiri. Woyera mtima wa Mulungu asavale zovala zimene zingapangitse kuti aliyense adzingomuyang’ana kapena zoonetsa kuti iye ndiye mwini makwacha. Mau akunena ndithu kuti chovala chidzikhala chosavuta kuchilongosola komanso chosadzikometsera kwambiri. Kukongoletsa ndiye kuti kuyika mwa dongosolo. Choncho zikutanthauza kuti kuchita zinthu mongoyesa kapena mosayikirapo mtima kulibe malo pa maonekedwe a mkhristu. Ana a Mulungu akuyenera kuti achite mwadongosolo kumbali ya mavalidwe, adzisamalire bwino ndi kudzikonza moyenera.

Kuvala modzilemekeza kuchokere pa chikhumbo chofuna kuchita chifuniro cha Mulungu

Mafashoni a kavalidwe koma ma sitayilo za kavalidwe zimabwera ndi kupita koma muyeso wa Mau a Mulungu susintha. Paulo anauza mpingo wa ku Roma

kuti: “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiwo” (Aroma 12:2). Mwana wa Mulungu safuna kukhumudwitsa mtima wa Atate ndipo amalimbikira chiyero chimene Mulungu amapereka mu gawo lokhudzana ndi mavalidwe kusiyana ndi kutsatira zimene dziko likupanga. Chenjerani ndi zimene dziko limayikapo mtima, popeza sizifanizidwa ndi Khristu. Zoipa zikuchulukira ndipo dzikoli likunka liwola kumbali ya makhalidwe. Mwana wa Mulungu ayenera kuyima payekha osakhazikika pa chidetso ndi kupusa kwake kwa dzikoli.

Ife sititsogozedwa ndi zilakolako za dziko lapansi

“Musakonde dziko lapansi, kapena za m’dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichili mwa iye. Pakuti chilichonse *cha* m’dziko lapansi, chilakolako cha thupi ndi chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo, sizichokera kwa Atate, koma kudziko lapansi” (1 Yohane 2:15-17). Zovala zambiri za masiku ano ndi zopereka chikoka ndipo zimaonetsa



gawo lobisika la thupi. Si azimayi okha, komanso ngakhale amuna akukakamidwa kuti adzivala molingana ndi fashoni ndiponso pofuna kusangalatsa thupi.

Zovala zimapangitsa munthu kuti adzione kapena achite mwa mtundu wina. Tayeserani kuwaveka ana

zovala za mitundu yosiyanasiyana ndipo mudzaone mmene amachitira ndi chovala chilichonse chimene avala. Anthu aakulu sasiyana konse ndi anawo ndipo ndi kofunikira kuti zovala zawo zikhale zimene zochokera mu mtima wamkati ndipo zikhale zokondweretsa Ambuye “Munthu asapeputse ubwana wako; komatu khala chitsanzo kwa iwo okhulupirira, m’mau, m’mayendedwe, m’chikondi, m’chikhulupiriro, m’kuyera mtima (1 Timoteo 4:12). Munthu woyera wa Mulungu avekedwe ndi mtima wamkati wa kudzilemekeza ndipo kenaka akhoza kuonetsera kunja mu zochita zake zonse.

Zokometsera ndi Zibangili kapena ndolo

1 Timoteo 2:9 amakaniziratu zovala ndolo za golide ndi zina za mtengo wapatali. Izi zikutsimikizidwanso pa 1 Petro 3:3: “Amene *kukometsera* kwanu kusakhale kwa kunja, kuluka tsitsi ndi kuvala za golide, kapena kuvala chovala;” Maweruzo a Mulungu anayikidwa motsutsana ndi ana aakazi a Ziyoni amene anali wodzikuzana ndipo amayenda monyada. Iwo amavala zokometsera zosiyanasiyana ndipo Mulungu analengeza chiweruzo pa iwo (Yesaya 3:16-24). Ndi kotsutsana ndi chifuniro cha Mulungu pamene anthu a mu mbadwo uno wa mu Chipangano Chatsopano adzivala zokometsera ndi zibangili kapena ndolo za mtengo wapatali. Zikhoza osakhala siliva kapena za golide komabe zikhoza kukhala zina za mtengo wake ndithu komatu izi zisutsana ndi mfundo ya kusadzikometsera kwambiri komanso chiyero. Ngakhale kuti zinthu zina sizinanedwe, Mau a Mulungu amafikira ku mbadwo uliwonse ndipo amakhudza chikhalidwe chilichonse. Pamene ana a Mulungu agwiritsa ntchito Mau, iwo amakhala ndi mzimu wakutha kusiyanita zabwino ndi zosakhala bwino ndipo ayenera kuwonetsetsa kuti asagwe mu msampha wa wongonenapo zilizonse ngakhale “zinthu zimene sizinatchulidwe mu Baibulo.”

Zodzoladzola ndi zopakapaka zodzikometsera

Chimodzimidzi, kugwiritsa ntchito zodzoladzola kapena zopakapaka kuti musinthe kawonekedwe ka thupi kapena nkhope yanu sizoyenera molingana ndi moyo wa chiyero. Zodzoladzola ngati fawundeshoni, lipisitiki, mascara, zopaka pamwamba pa chikopa cha diso, zopaka pa zikhadabo, zodzibayabaya pakhungu komanso kulembalemba zithunzi pakhungu ndi zina

(Yapitirira pa tsamba 8)

Woyera
mtima wa
Mulungu
adziveke ndi
mzimu
wamkati wa
kudzilemekez
a umene
kenako
udzaonekera
mu zonse
zimene iye
akuchita.

Kopanda
muyeso,
chiphunzitso
chidzakhala ngati
chitini chopanda
kanthu ndipo
mapeto ake
phindu la
chimene
mukuchita
silioneka.

(Kuchokera pa tsamba 7)

zotere zatchuka kwambiri padziko lino, ndipo zimenezi ndi ntchito za thupi ndipo siziyandikirako pa kusachita manyazi ndi kuoneka modzilemekeza. Matupi athu ali kachisi wa Mzimu Woyera. Ambuye atithandize osati tingokhala mu choonadi ichi, komanso kuti tichiphunzitse kwa ana aang'ono ndi achinyamata.

Masitayilo a tsitsi


Kukonza tsitsi kumatenga nthawi ndithu. Ngakhale kuti mitundu yosiyanasiyana ya anthu ili ndi masitayilo osiyanasiyana a tsitsi, malemba amapereka mfundo zakuti titsatire. “Kodi ubadwidwe womwe sutiphunzitsa kuti ngati mwamuna aweta tsitsi chinyozetsa iye? Koma ngati mkazi aweta tsitsi, kuli ulemerero kwa iye; pakuti tsitsi lake lapatsidwa kwa iye ngati chophimba” (1 Akorinto 11:14-15). Mulungu amasangalala ndi kumvera mau ake ndipo malemba amanena mwa chimvekere kuti mwamuna adzikhala ndi tsitsi lalifupi ndipo tsitsi lalitali la mzimayiyo (monga mmene Mulungu anaperekera) limamuphimba komanso kuonetisa ulemerero wake.

Mametedwe a tsitsi kwa mzimayi komanso njira imene mzimayi angasamalire tsitsi lake zidzikhala zoyenera ndi zosadzikometsera kwambiri. Monga mmene tanenera kale, kuluka kwa tsitsi kapena zolukira tsitsi ndi zinthu zina zoyika mu tsitsi ndi zoletsedwa.

Musaweruze

Muyeso wa anthu a Mulungu udzikhala pamwamba pa muyeso wa dziko umene ukusuluka. Maweruzo asamatengere pa anthu ena koma pa muyeso wokhazikika wa Mau a Mulungu, popeza Mauwo ndi amene adzatiweruze pa tsiku lomaliza (Yohane 12:48). Mwana wa Mulungu aliyense ayenera kufunitsitsa kuti atsogozedwe ndi Mzimu wa Mulungu, pozindikira kuti Mzimuyo sadzatitsogolera

Walitsani Msewuwo;
Tolani miyalayo;
Muyike muyeso kwa Anthuwo.



mosemphana ndi Mau a Mulungu. Pa nyengo ino imene zauzimu zikupeputsidwa, “Pakuti sitilimba mtima kudziwerenga, kapena kudzilinganiza tokha ndi ena a iwo amene adzivomeretsa okha; koma iwowa, podziyesera okha ndi iwo okha, ndi kudzilinganiza okha ndi iwo okha, alibe nzeru... pakuti si iye amene adzitama yekha, koma iye amene Ambuye amtama ali wovomerezeka.” (2 Akorinto 10:12,18). Munthu asalalitse kuti asaweruze chipulumutso cha mnzake pongoona zochitika kunja popeza alipo anthu ena amene sanayambe amvapo choonadi cha chiphunzitso. Ndi chokhumba cha Mulungu kuti onse afike pozindikira kuwala kumeneku.

Mudziyikire nokha Muyeso

Ndi kofunikira kwambiri kuti oyera mtima akhale ndi miyeso imene iwo adzitsatira pa moyo wao wa tsiku ndi tsiku. Popanda muyeso, chiphunzitso chimakhala ngati chitini chopanda kanthu ndipo pamapeto ake phindu la chimene mukuchita silioneka. Baibulo silinakambe tchutchutchu za mmene direni likhalire kapena kutalika kwa manja a chovala. Komabe, podziwa kuti maliseche amayamba pamene mwaonetsa kena kalikonse kamene kali kumtunda kwa bondo, ndi zomveka ndithu kuti muyeso umene

tingawutsatire ndiwakuti chovala chivundikire mawondo bwinobwino komanso ngati chili ndi mkono, ukhale wotalika bwino. Pamwamba pa zonse, anthu afunika kulandira mavumbulutso paokha kuchokera kwa Mulungu kuti choonadi ichi achilandire nkukhala chaochao. Pali kutayirira ndi chisokonezo chochuluka ngakhale pakati pa oyera mtima athu ponena za nkhanayi. Kodi nanga ndi ndani amene adzayankha kuyitana ndi kulangiza kwa Mulungu kopezeka pa Yesaya 62:10? “Pitani, pitani pazipata; konzani njira ya anthu; undani, undani khwalala; chotsani miyala, kwezani mbendera ya anthu.”

Chimwemwe mu Kumvera

Pali njira yaikulu ya chiyero imene ipambana njira zonse za dziko lino lochimwali. Muyeso wakunja wa chiyero, monga momwe Mulungu waperekera, ndi wokongola. Kudzipatsa ulemu sichinali chinthu chimene chimayenera kuwaika anthu mu goli. Chiyero choonekera kunja ndi chimodzi mwa zotsatira za mtima ndi moyo wangwiro. Malamulo okha amabweretsa imfa, koma Mzimu amapatsa moyo ndi cholinga ku Mauwa “Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake: ndipo malamulo ake sali olemetsa” (1 Yohane 5:3). Ndi chinthu chopatsa chimwemwe kwa mkristu pamene atsatira Mau a Mulungu. Zokoma zimene timazilandira pa kumvera zimaposa nsembe zina zilizonse zimene tingazipereke kwa Ambuye. Maonekedwe akunja a anthu a Mulungu adzionetsa kuti iwo ndi mzika za ufumu wa Kumwamba.

—mws

Kodi Ndichivale?

(Mafunso oyenera kufunsa okhudzana ndi maonekedwe akunja)

- Nchifukwa chiyani ndikufuna kuchivala?
- Kodi ndimaoneka bwanji ndikachivala?
- Kodi thupi langa laphimbika? Kodi ndi choonetsa thupi kapena ndi chothina kwambiri?
- Kodi chili choyenera ndi chaulemu?
- Kodi ndikupereka chithunzi chotani ku dzikoli?
- Kodi chikuonetsa kudzichepetsa ndi kusadzikometsera koonjeza?
- Kodi Mulungu akusangalala nacho?

CHIKHALIDWE



Pali kusiyana ndipo padzakhalabe kusiyana kwa kavalidwe ndi ma sitayilo a mavalidwe chifukwa cha kusiyana kwa zikhalidwe. Dziko limodzi lidzasiyana ndi linzake komanso mbadwo umodzi udzasiyana ndi wina wotsatirawo. Ngakhale kuti Mau a Mulungu sanena kuti anthu adzivala motere, komabe mfundo zimene Mauwo amapereka zimaposa zikhalidwe ndi miyambo yonse. Ngati chovala chimene chili chovomereza pa chikhalidwe china chitsutsana ndi Mau a Mulungu, pamenepo mavalidwewo agonjere ku Mau a Mulungu. Mzimayi wa ku Amerika akhoza kuvala siketi ndi bulawuzi, ndipo wa ku Malawi angathe kuvala chitenje pamene wa ku Pakistan akhoza kuvala

chovala chopimba thupi lonse chovala chotchedwa shalwar kameez. Mavalidwe onsewa ngakhale ali osiyana akhoza kukhala ovomerezeke pamaso pa Ambuye malingana ngati ali olemkezeke, aatali bwino, aulemu, oyenera ndi adongosolo.

Pali nthawi komanso zidzakhalapo nthawi zimene chovala china chiyimira zinthu zina pa nyengo ina mu mbiri ya mtundu wa anthu wina wake. Pokhapokha atadziwa tanthauzo lake, mwana wa Mulungu adziletse kuvala chovala chimene uthenga wake uli wosalemekeza Mulungu. Mwa chitsanzo, lerolo, wina atavala chovala cha mtundu wa buluu kuyimira gulu limene limagwirizana zakuti amuna kapena akazi adzikwatirana okhaokha, sichingakhale chanzeru kuti woyera mtima wa Mulungu avale choterecho. Mfundo yofunika kuyigwira ndiyo yakuti pamene zaka 40 zapitazo kuvala malaya a buluu zinalibe tanthauzo lenileni, mpingo sukuphunzitsa kuti ndi cholakwika kwa munthu ngati asiya kuvala malaya a mtundu wa buluu.

—mws



Funso: Kodi thalauza ndi chovala choyenera kwa mzimayi?

Pofuna kuyankha funsoli, tiyeni tiwunike mozama mau a pa 1 Timoteo 2:9: “Momwemonso, akazi adziveke okha ndi chovala choyenera, ndi manyazi, ndi chidziletso . . .”

“Chovala choyenera” mu chinenero cha ch Griki ndi “*kósmios katastole*.” Ndipo buku la *Vine's Expository Dictionary of New Testament Words* limanena kuti kuvala moyenera, *kósmios*, ndiko kolongosoka, kwadongosolo, kodzipatsa ulemu, kodzilemekeza. Kuvala modzilemekeza molingana ndi baibulo kumakhudzananso ndi mkhalidwe wa munthu.

Mau a chiGriki akuti *Katastole* onena za chovala amachokera ku mau awiri *kata* ndi *stole*. Mau akuti *Kata* amatanthauza panso chovala chofika mmunsi pamene *stole* ndi chovala chachitali, chosagwira thupi chovalidwa kunja, chofundira. Choncho *Katastole* atanthauza “kutsitsa, chotsika, chovala chimene chili chachitali bwino chovala, mavalidwe” (*KJV New Testament Greek Lexicon*). *Katastole* tingathe kunena kuti ndi “Chovala chachitali kapena mkanjo chofika mpakana ku mapazi” (*The Complete Word Study Dictionary, Zodhiates*).

Wotambasula nkhani dzina lake Adam Clark akunena zimene akudziwa pa za *katastole*:

Mtumwiyu apa akukhala ngati akunena za mavalidwe osiyanasiyana a chovala chi Griki ndi chi Roma. Poyambirira chovala cha stola chinali chopanda zokometsera zilizonse. Inali nsalu yaitali, yopindidwa chapakati, ndipo yosokedwa mbali zonse ziwiri, ndikungosiya malo akuti pakhoza kulowa mkono. Chakumtunda kwake inali yodulidwa kapena kusiya malo akuti mutu ukhoza kulowa. Chinali chachitali mpaka kufika ku mapazi mbali zonse ziwiri, kutsogolo ndikumbuyo komwe, ndipo chapamimba pamadutsa chingwe chimene chimagwira malayawo. Chingwecho dzina lake linali zona ndipo chimakhala mmunsi mwa mabere. Nthawi zina chimakhala ndi mkono komanso nthawi chimakhala chopanda. Komanso kuti mkono usavute kudutsa, chimawunjikidwa malo amodzi cha paphepapa ndikumangidwa ndi lamba kapena chingwe. Azimayi ena a chi Griki amavala chovalachi ataching'amba mbali zonse ziwiri kuyambira panso mpaka kufika m'mwamba mwa mabondo kuti mbali ina ya ntchafu lionekere. Izi zimatchedwa mawawa amvula kapena zionetsa ntchafu, komabe amavala anali atsikana aang'ono ndi zimayi ena opanda mwambo.

Zikuoneka ngati *katastole* anali chimodzimidzi ndi chofundira, chimene chimapangidwa pafupifupi ngati stola, ndipo chimafika mchiuno, kutsogolo ndi kumbuyo komwe, ndipo nsalu ina imadzadzana pa phewa itamangidwa ndi chingwe kapena lamba, ndipo pamwamba pake imakhala ndi bowo kapena amaying'amba pamwamba kuti mutu ukhoza kutulukira mosavuta, ndipo imalendewera pa stola, inali payokha osadaliranso zona kapena lamba uja. Ma Griki sanakwanitse kupanga chovala chaulemu ndi cholemekezeka. Izi zinachitika ku Mangalade m'chaka cha 1805 pamene anafuna kupanga chovala chosavuta kuvala, chaulemu, ndi chokongola. Mmalo mwake chovala cha manyado ndi chopanda tanthauzo lenileni chinapangidwa. Chimenechi sichinakhalitse ndipo nachonso chinasiyidwa.

Muyeso wa mavalidwe kwa mzimayi malingana ndi Baibulo ndiwo wakuti avekedwe mu “*kósmios katastole*”—chimene chili chovala cholemekezeka, chaulemu, chachitali bwino, chotaya komanso chofika kumapazi. Chovala chokhala ndi miyendo monga thalauza limene sizifika panso komanso



zosataya. Choncho, ma thalauza, ma mini, madiresi aafupi, zovala zothina ndi zina zotere sizili zopatsa ulemu ndi zosayenera kwa mzimayi amene akunena kuti amalemekeza Mulungu.

Kuonjezera pa chiphunzitso chimene Malemba amapereka pa kuvala modzilemekeza, ndi kofunika ndithu kuganizira agawo ena a nkhani iyi ya akazi kuvala thalauza, chimene chili chovala cha amuna. Chipangano Chakale chimaphunzitsa kuti mkazi asavale chovala icho chimene chili cha mwamuna. (Duteronomo 22:5).

“Zovala zokhala ndi miyendo” Uwasokerenso zovala za miyendo za bafuta wa thonje losansitsa kubisa maliseche ao; ziyambire m’chuuno zifikire kuntchafu. Zinali mtundu wa chovala chokhala ndi mphanda chimene ansembe amavala mu Chipangano Chakale (Eksodo 28:42). Malingana ndi kalozera wa chinenero cha chi Heberi mauwa atanthauza “thalauza limene limafika m’kawondo, kapena kungodutsa pang’ono kapena kufika mu akakolo.” Mu nthawi ya Baibulo, azimayi samavala zovala zokhala ndi miyendo kapena mphanda. Izi zakuti azimayi adzivala ma thalauza zinayamba mzaka za ma 1900 ku ulaya kwa azungu. Pa nthawi ya nkondo za dziko lonse, pamene amuna awo anapita ku nkondo, azimayi anachoka m’makomo mwao nkuyamba kugwira ntchito m’mafakitale ndi malo ena ndipo chifukwa cha ichi ambiri anayamba kuvala thalauza pogwira ntchito. Pamene chinabwera chi feminism chimene chimalimbikitsa ufulu wa azimayi, azimayi ambiri anakamizidwa kusiya udindo wao ngati “osunga pakhomo” ndipo anayamba kulimbirana ntchito ndi azibambo mu ma ofesi ndi malo ena ogwira ntchito komanso ngakhale pa zochitika zina zonse. Maudindo amene Mulungu anapereka kwa abambo komanso kwa amayi panyumba ndi mu zochitika zina anaphwanyidwa. Kuvala ma thalauza kwa azimayi ndi gawo limodzi chabe limene likukamba za mzimu umene ukutsogolera chi Feminism. Kuvala thalauza chinali chizindikiro cha ulamuliro, choncho funso ndilo lakuti: “Kodi ndani amavala thalauza m’banja?” Tsoka lake ndilo lakuti chiyero cha anthu ambiri chasokonezedwa ndi maganizo a chi Feminism amene ali otsutsana kwambiri ndi zimene Malemba amaphunzitsa.

Mulungu analenga amuna ndi akazi mosiyana ndipo amayembekeza kuti adzione monga mmene aliri osafuna kufanizira ndi anzawo. Dzikoli likuyesetsa kuchita zotheka kuti pasaoneke kusiyana kulikonse pakati pa amuna ndi akazi ndipo mavalidwe ndilo gawo liomodzi limene izi zikuoneka. Pa dziko lino, chizindikiro chimene chimayikidwa ku mabafa a amuna ndi cha munthu atavala thalauza ndipo ku mabafa a akazi amayika chithunzi cha munthu atavala diresi. Dzikoli ngakhale lasochera mu zinthu zambiri chifukwa cha uchimo, komabe limazindikira kuti pali kusiyana ndithu pakati pa amuna ndi akazi.

Thalauza linali chizindikiro cha ulamuliro, choncho Funso ndi lakuti: “Kodi angavale thalauza m’banja ndi ndani?”

Pa chikhalidwe cha kwa azungu, azimayi amene avala modzipatsa ulemu amaonekera mwansanga pakati pa anthu, komabe amadziwika ngati anthu achiyero. Izi zikutiphunzitsa kenakake kuti ngakhale dziko limene limamuona mzimayi wovala modzilemekeza ngati mkhristu wachiyero.

Kwa zaka pafupifupi 6,000 amayi amavala ma diresi aatali ndi zovala zokhala ngati mikanjo. Ndi posachedwapa, mu zaka 100 zapitazi pamene kuvala madiresi zakhala ngati zosayenera kwenikweni pakati pawo. Nkofunikira kudziwa kuti ngakhale pakati pathu lerolo, ngati munthu wamayi akufuna kuti adziwikedi kuti ndi mzimayi ndi kuonetsa chikhalidwe ngati mkazi, amavala diresi.

Mau a Mulungu sanasinthe ndipo njira yake ikadali yolondola ndi yangwiro. Nkofunikira kuti amuna ndi akazi achikhristu adzichita zinthu ngatidi akhristu ndipo akhale pa malo oyenera amene Mulungu anawapatsa. Ngakhale kuli kutsutsana ndi Malemba kwa mzimayi kuvala thalauza, mzimu umene umapangitsa zimenezi ndi wolakwika kwambiri. Ambuye apereke masomphenya ndi mzimu wozindikira kwa anthu ake kuti potero akhoza kukhala kuwala mpaka pa tsiku limene lwo adzabwerenso.





KODI MUKUDZIWA?

Kodi kuvala nsapato za gogoda ndi kogwirizana ndi chiphunzitso chopezeka m’malemba cha chiyero, kudzipatsa ulemu ndi kudzichepetsa? Tiyeni tiwasiye mau eniake ayankhe okha funso limeneli.



“Komatu gogoda zimakoka akatumba... apodi ndiye mukunena zoono. Nsapato za gogoda sizimangokutalikitsani, komanso kayendedwe kanu kamasintha komanso mmene mumadziwonera zimasintha... Mumadziona kuti mwayimira ndipo muli wopambana kuposa onse. Ndipo ngati thupi lanu limva choncho., nkosavuta kuchita moteromo..”

—“Why a Vogue Editor Will Always Wear High Heels” wolembe - Alexandra Shulman.



Mau a pa
Nyengo Yake

Kupatulidwa kukanena Uthenga Wabwino

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.org


CHIYERO CHA KWA AMBUYE

“Paulo, kapolo wa Yesu Khristu, mtumwi waitanidwa, wopatulidwa kukanena Uthenga Wabwino wa Mulungu.” —Eksodo 1:1

Palibenso maitanidwe ena aakulu kuposa kukhala mtumiki wa Yesu Khristu. Ndi chinthu chaulemu komanso cha mwayi kuchita zimene akufuna Mfumu ya Mafumu komanso Mbuye wa Ambuye mmalo mongotsata zinthu za dziko lapansi. Kulalikira kwa osochera ndi a banja la chikhulupiriro si ntchito kapena chimene munthu anasankha kuti adzichita, koma ndi maitanidwe ochokera kumwamba kwa Mulungu.

Mzimu wa Ambuye akuitanabe oyera mtima ku ntchito ya utumiki. Ngakhale kuti maitanidwe aliwonse a Mulungu amakhala osiyana. Iye akufunabe anthu amene apereke kwathunthu mtima wawo, nthawi yawo, ndi mphamvu zawo ku ntchito yolalikira Uthenga Wabwino. Paulo anapatulidwa kukanena Uthenga Wabwino wa Mulungu. Iye anaitanidwa kusiya njira ya dziko lino ndipo anapatulidwa kuti akakwaniritse maitanidwe a utumiki wathunthu. Pakhoza kukhala nthawi ndi malo mwa Ambuye pamene tikhoza kutumikira kwa kanthawi koma sipadzakhala nthawi imene tidzadzikhuthula kwa kanthawi. Mu mbadwo wathu wa lero pakufunika kuti atumiki a Mulungu adzipatule ku zosamalira za moyo uno zimene zimawapangitsa kuti amangike ku dziko lino ndipo wokha adzipereke kwathunthu ku ntchito za uthenga wabwino kumudzi kwawo komanso kunjira kwa dziko lawo.

Ngati mwaitanidwa ndi Mulungu ndipo mwapatulidwa ku Uthenga Wabwino, mulimbe mtima ndipo mukhale okhulupirika mu nthawi ya kusowa, popeza Mbuye wanu adzakusamalirani.



—mws